




MUTU 9:

UTUMIKI
WOYAMBIRIRA



ONANI,
MWANAWANKHOSA
WA MULLINGU AMENE
ADZACHOTSA
MACHIMO A DZIKO
LONSE LAPANSI.

AMEN
EYU NDI
MESIYA!

IYE AMENE
ANENERI
ANANENA ZA
IYE.

ADZACHITA
CHIYANI?



KOMA
SINDINGAKUSIYENI,
AMBUYE.

TSATANI
YESU.

INE SINDINE MBUYE WANU.
NDIYENERA KUCHEPA KWAMBIRI
NDIPO IYE AYENERA KUKULA MPAKA
KUKHALA WAMPHUMPHU. IYEYU
NDIYEDI MESIYA, MPULLUMUTSI WA
DZIKO LAPANSI. MTSATENI.

AMBUYE, TIDZAKUTSANI
NDIPO TIDZAKHALA OPHUNZIRA
ANU. MUMAKHALA KUTI?

BWERANI
MUDZAONE.





**FILIPO,
NDITSATE.**

**INDE AMBUYE,
TAKHALA TIKUKUDIKIRANI.
KOMA POYAMBA NDIPITE
NDIKAPEZE *NATANAELE*.**

**IYENSO,
WAKHALA AKUTSATIRA
MALAMULO A MULLINGU
NDIPONSO KUDIKIRA
MESIYA.**



**NATANAELE
ALI KUTI?**

**ALI M'MUNDA.
KWAGWANJI
KODI?**

**AI, ZONSE ZILI
BWINOBWINO.**




NATANAELE,
ULI KUTI?

NDILI
PANO,
MBALE
WANGA.

NATANAELE,
TAMPEZA IYE AMENE
MOSE NDI ANENERI
ADALEMBA ZA IYE, YESU
WA KU NAZARETE,
MWANA WA
YOSEFE.

**MESIYA? MWAYANKHULA
NAYE? KOMA NAZARETE?
PALIBE CHABWINO CHOMWE
CHINACHOKERAPO KU NAZARETE.
MESIYA ANGACHOKERE BWANJI KU
MALO OSAUKA NDI ACHABECHABEWO?
ADAYENERA KUBADWIRA
M'BETELEHEMU WA YUDEYA.**




**TIYE
UKADZIWONERE
WEKHA. YOHANE
ADACHITIRA LUMBONI
ZA IYE, NDIPO
ANDIREYA ALI NDI
IYEYO.**



ZOONANDI,
LIYU NDI MWISRAELE
WOYERA MTIMA.

FILIPO, KODI
UNAMUUSA
CHILICHONSE
CHOKHUDZA
MOYO
WANGA?

NCHIMODZI
CHOMWE.



SIMUNDIDZIWA.
MUNGANENE BWANJI
KUTI NDINE WOYERA
MTIMA?

FILIPO ASANAKUITANE,
PAMENE UNAKHALA PANSI
PA MTENGO WA MKUYU,
NDINAKLUONA PAMENEPO.

MUNANDIONA
BWANJI?
PALIBETU AMENE
AMADZIWA
KUMENE
NDINALILI.




NDINU MWANA
WA MULLINGU.
NDINU MFUMU
YA ISRAELE.

KODI ICHI WADZIDZIMUKA NACHO?
UDZAONA ZODABWITSA ZAZIKULU KUPOSA
CHIMENECHI. UDZAONA KUMWAMBA
KUTATSEKUKA, ANGELO A MULLINGU
AKUTSIKA NDI KUKWERA PA INE. BWERA.
PALI ZAMBIRI ZOTI TICHITE.

YOHANE 1:45-51


ANDIREYA NAYENSO
ANANKA NAYANG'ANA
MBALE WAKE KUTI
AMUZE ZA YESU.



SIMONI, TAMPEZA
MESIYA AMENE
YOHANE ANANENA
ZA IYE.

TIYE
UKAONE.

LITI? KUTI?
NGOONEKA BWANJI?
KODI PALI ENA AMENE
AKUMUTSATIRA?




**IWE NDIWE
SIMONI MWANA
WA YONA, KOMA
LDZATCHEDWA
PETRO.**

**NDISIYIRA A
M'BANJA MWANGA
BWATO LANGALI NDI
KUKUTSATANI.**



POSAKHALITSA YESU ANASANKHA AMUNA 12 KUTI
AZIMUTSATIRA NDI KUMAMVA ZIPHUNZITSO ZAKE.
PAMBUYO PAKE AMUNAWA ANATCHEDWA KUTI
OPHUNZIRA 12. ANAPITA M'MIZINDA YOSIYANASIYANA
KULALIKA LITHENGA WABWINO WA LIFUMU.



YESU NDI OPHUNZIRA
AKE ANAPITA KU KACHISI
KUKAPEMPHERA, KOMA
KACHISIYO ANADZAZA NDI
ANTHU OGULITSA MALONDA.

NDIYISINTHIRENJI
NDALAMA YANGA
NDISANAKAPEREKE KU
KACHISI? ZIKUONEKA
KUTI MUKUMAPEZA
PHINDU LOCHULUKA.

ANSEMBE
ASOKONEKERA.
AMAFUNA KUPEZA
PHINDU PA
CHILICHONSE CHIMENE
CHAGULITSIDWA
M'KACHISI.

ANSEMBE
AMAVOMEREZ
A ZIMENEZI.

YOHANE 1:40-42, 2:12-14; MARKO 3:16



AKUCHITA CHIYANI?
WAKHALA AKUNGOYANG'ANA;
WAIMA PAMENEPO KWA ORA LIMODZI,
SAKUNENA KANTHU, AKUNGOLUKA
CHINA CHAKE.

TAPEZA PHINDU
LOCHULUKA LERO. IZI
NZABWINO KUSIYANA
NKUMAGWIRA NTCHITO
YOLIPIDWA.




**CHIKWAPU!
AKLIKWAPULA!**



**NYUMBA YA ATATE
ANGA IYENERA KUKHALA
MALO A MAPEMPHERO, KOMA
MWAISANDUTSA PHANGA LA
ANTHU AKUBA. TULUTSANI
ZONSEZI. TSOPANO!**

**NYUMBA YA
ATATE AKE!
AKUDZIYESA NDANI?
MESIYA?**



NYUMBA YA
ATATE ANGA
ISASANDUKE MSIKA.
NDINU MBAVA
ZOTHERATU.

KHOOO!

YOHANE 2:15-16



KHWAPU!

NDINU
MBADWO WA MPHIRI.
MUMALANDA CHAKUDYA
AMAI AMASIYE.

KODI
AKUGANIZA
KUTI IYEYO
NDIYE WOPOSA
ANZAKE?

MAYOOO!



MATEYU 6:5-7, 12:34;
YOHANE 2:15-16; 1
TIMOTEO 6:10

PHOPHOPHO!!!

GWENGWEREREII

CHIFUKWA
CHA CHINYENGO
CHANU
MUMAPEMPHERA
MAPEMPHERO
ATALIATALI.

KWAPU!!!

SIMUKONDA
ANZANU,
MUMAKONDA
NDALAMA ZA
ANZANU.




TSIKU LINA
MUKADZABWERAN
SO KU NYUMBA YA
ATATE ANGAYI
MUZIDZAILLULA
MACHIMO ANU.



KODI
MUKUKUMBUKIRA
PAMENE DAVIDE
ADAYANKHULA
ZOKHUDZA MESIYA?

PAJATU ALEMBI
A MALAMULO
AMATIPHUNZITSA KUTI
PAMENE MESIYA
ADZABWERA, ADZAFIKA
MWADZIDZIDZI KU
KACHISI WAKE.

INDE, CHIDWI
CHANGA PA NYUMBA
YA MULLINGU
CHIDZANDINYEKEZA
CHIFUKWA ADANI A
MULLINGU AIWALA
MAU A MULLINGU.



NDIYESA NDIWE
YESU WA KU NAZARETE
AMENE YOHANE AMANENA.
WASAUTSA ANTHU LERO.
UTISONYEZA CHIZINDIKIRO
CHANJI?

CHIZINDIKIRO CHOTI
NDINE MESIYA CHIDZAONEKA
MUKADZAONONGA KACHISI
UYU. PA MASIKU ATATU
NDIDZAMUMANGANSO.




KACHISIYU
ANAMANGIDWA KWA
ZAKA 46, NDIPO
LUKUGANIZA KUTI UKHOZA
KUMUMANGANSO PA
MASIKU ATATU.
UMENEWU NDI
MWANO!

UKADZABWERANSO
KUNO
TIDZAKUMANGA.

YESU AMANENA ZA KACHISI WA THUPI
LAKE. KOMA SANAWAMASULIRE, POPEZA
SANKAFLINA KUTI IWO AMVETSETSE.

YESU NDI OPHUNZIRA AKE ANACHOKA KU
YERUSALEMU NABWERERANSO KUMPOTO
KU NAZARETE, KWAO KWA YESU.



OO, **YESU**,
WABWERA KWANU.
LIBWERE NDI ANZAKO ONSE
NDIPO NDIDZAWAKONZERA
CHAKUDYA CHOKOMA.

AMAI,
SITIKHALITSA
KUNO - IKATHA
SABATA
TIZINYAMUKA.




TAKONDWA KWAMBIRI
POONA MMODZI WA IFE ATABWERERA
KWAO NDI ABWENZI AKE. TAKHALA TIKUMVA
ZODABWITSA ZA IWOWA. TIKUFUNA
TIMVE ZAMBIRI BWINO LINO.

KOMA TSOPANO,
YESU, KODI
LINGATIWERENGEREKO
MALEMBO OYERA PA
TSIKU LA LERO?


MONGA MWA
CHIZOLOWEZI CHAKE,
YESU ANAPITA KU
SUNAGOGE, KUMALO
KUMENE AYUDA
ANKAPEMBEDZERAKO
PA SABATA.*

LUKA 4:16-21 *SABATA NDI TSIKU LOPEMBEDZA PA MLINGU
ULIWONSE LIMENE MULLINGU ANALIKHAZIKITSA PA TSIKU LACHISANU
NDI CHIWIRI, NDIPO ADALIKA KUKHALA LIMODZI MWA MALAMULO AKE
KHUMI AJA KWA AYUDA (GENESIS 2:2-3; EKSODO 20:10).



YESU ANATSEKULA
BUKU LA MNENERI
YESAYA NAPEZA UNENERI
WODZIWIKA BWINO
WA MESIYA.

"MZIMU WA AMBUYE ULI PA INE,
CHIFUKWA WANDIDZOZA KUTI NDILALIKE
LTHENGA WABWINO KWA ANTHU OSAUKA,
NDI KUPENYETSA AKHUNGU, KUMASULA
OMANGIDWA, NDI KULENGEZA KUTI NTHAWI
YAKWANA KUTI MULLUNGU ABWERETSE
CHIPULLUMUTSO KWA ANTHU AKE."



LERO LINO
UNENERI UWU
WAKWANIRITSIDWA.

SUNAGOGE INALI NYUMBA IMENE AYUDA
ANKAKUMANAMO PA SABATA KUTI
APEMBEDZE MULLINGU PAMODZI.
INKAGWIRITSIDWANSO NTCHITO PA ZINA
ZA CHIKHALIDWE CHAO KOMANSO NGATI
SUKULU. SABATA LINALI TSIKU LOMALIZA
PA MLINGU ULIWONSE, AYUDA
ANKALILEMEKEZA TSIKULI NDIPO
SANKAGWIRA NTCHITO ILIYONSE.



**KUCHITIRA MWANO
MULUNGU!**

**IWE
NDIWE
MWANA WA
MMISIRI WA
MATABWA.**

**KHALANI
CHETE.
TIKUPITA.**

**MGENDENI
KUTI AFE.
AKUDZIYESA
MESIYA!**


YESU NDI OPHUNZIRA AKE ANAPITA
KU KAPERNAO, MZINDA UMENE UNALI
M'MPHEPETE MWA NYANJA YA
GALILEYA, KUMENE KUNKAKHALA
OPHUNZIRA AKE ENA. KUMENEKONSO
ANAKALOWA M'SUNAGOGE.



NDIPO MNENERI ADATI
MESIYA ADZAKHALA KUUNIKA
KWA ANTHU A MITUNDU INA
NDIPO ADZAMUKHULLUPIRIRA.
WODALA NDI MUNTHU WOYERA
MTIMA, CHIFUKWA ADZAONA
MULLINGU. MULLINGU SANYOZA
ALIYENSE WODZA KWA IYE,
KAYA MYUDA KAPENA MUNTHU
WA MTUNDU WINA.




**WOYERA LIJA.
TISIYENI.**



NDIKUKUDZIWANI.
NDINU WOYERA UJA
WA MULLINGU.

ALI NDI
ZIWANDA.
MTULUTSENI.



**KODI MWABWERA
KUDZAONONGA
ZIWANDAFE, NTHAWI
YATHU ISANAFIKE?
TISIYENI.
TAKULAKWIRANINJI?**

**NDANI
ANAMULOLA KUTI
ALOWE MUNO!
TAONANI! NDI
WOOPSA.**



ZIWANDA,
NDIKUKULAMULANI
KUTI MUTULUKE MWA
MUNTHUYU NDIPO
MUSADZAMUVUTITSE
NSO.

LUKA 4:28-35



TULUKANI!!

EEEEEE!!!



MWAMUTANI?

KODI
WAFWA?



KENAKA MWADZIDZIDZI,
ANAIMIRIRA.

TAMANDANI
MULLINGU!

ZIWANDA ZAPITA.
WAMASULIDWA.
TSOPANO PITA
KWANU NDIPO
USAKACHIMWENSO.

YESU ALI NDI
ULAMULIRO WONSE
PA MIZIMU YOIPA.
MUNTHU UJA
WACHIRA.



TIBWERA.

PETRO,
MKAZI WAKO
AKUTI UPITE
KAYE KU
NYUMBA.
AMAI AKE
AKUDWALA
MALUNGO
KWAMBIRI.



IWE PETRO,
MWAMLINA WANGA,
NDIKUCHITA MANTHA
KWAMBIRI.
MALLINGOWA
AKUNGOKULIRAKULIRA.

OSACHITA
MANTHA.
AMBUYE ALI
POMPANO.

MARKO 1:25-28; LUKA 4:35-38




DZUKANI MAI,
MWACHIRITSID
WA.



**AKUDZUKADI!
ACHIRITSIDWA!**

ANADZUKA PAMENE
ADAGONAPO NATUMIKIRA
YESU NDI OPHUNZIRA AKE.



NKHANI YA
KUCHIRITSIDWA KWA
MAIYO INAWANDA
NDIPO ANTHU
ANABWERETSA KWA
YESU ODWALA AMBIRI.

AMBUYE, ABAMBO
ANGA ADALUMALA PAMENE
NDINALI MWANA WAMNG'ONO
KUFIKIRA LERO LINO.
MTENGO UNAWAGWERA NDI
KUWATHYOLA MSANA.
NGATI MUFUNA,
TITHANDIZENI.

*DZUKANI
MUZIPITA.*





**NDIKLUTHA
KUYENDA!
ZODABWITSA
NDITHU!**

**AMBUYE, MWANA
WANGA WAMKAZI
ANABADWA
WAKHUNGU, KODI
MUKHOZA
KUMUTHANDIZA?**

MARKO 1:30-34; LUKA 4:38-40

MONGA MALEMBO
AMANENERA, 'AKHUNGU
ADZAONA.' MWANA WANU
AKUTHA KUONA
TSOPANO.





**ABABA, KODI
NDINUYO?**

ABABA, SINDINKADZIWA
KUTI MUMAONEKA
CHONCHI. KOMA NDINU
OKONGOLA KUSIYANA NDI
MMENE NDINKAGANIZIRA.




YESU NDI OPHUNZIRA AKE
ANAPITA KU YERUSALEMU PA
NTHAWI YA CHIKONDWERERO
NDIPO YESU ANAPHUNZITSA
M'NYUMBA YA MULLINGU.



WINA AKAKUTEMBERERANI,
MUSAMABWEZERE TEMBEREROLO,
KOMA MUZIPEMPHERA KUTI MULLINGU
AMUDALITSE. MUZIWACHITIRA ANZANU
ZIMENE MUNGAKONDE KUTI ENA
AKUCHITIRENI.



A man with a beard, wearing a white tunic and a yellow shawl, stands on a raised platform in a classical building with columns. He has his right hand raised and is speaking to a crowd of people below. The crowd consists of men and women in various head coverings and robes. A speech bubble is positioned in the foreground, containing text in a local language.

MUDAMVA KUTI ANTHU
AKALE ANKATI MUZIKONDA
ABWENZI ANU NDI KUMADANA
NDI ADANI ANU, KOMA INE
NDIKUTI MUZIKONDA ADANI
ANU NDI KUMAWACHITIRA
ZABWINO.



ANZANU AKAKUCHIMWIRANI,
MUZIWAKHULULUKIRA. MUKAKHALA
OYERA MTIMA MUDZADALITSIKA, POPEZA
MUDZAONA MULINGU. MUKAMAKHALA
MWAMTENDERE NDI ANZANU,
MUDZADALITSIKA KOPOSA.

NANGA ZIJA ZOTI
DISO KULIPA DISO NDI
DZINO KULIPA DZINO?



MUNTHU AKAKUMENYANI PA TSAYA,
MUMUPATSE TSAYA LINALO KUTI ALIMENYENSO.
MUSAMAKONDA CHIWAWA. NGATI MNZANU ALIBE
CHOVALA NDIPO INU MULI NDI ZOVALA ZIWIRI,
MUMPATSE CHOVALA CHIMODZI MNZANUYO. NGATI
ALI NDI NJALA, MPATSENI CHAKUDYA. ATATE ANU
AKUMWAMBA ADZAONA NTCHITO ZANUZO
NDIPO ADZAKUDALITSANI.



MUDAMVA KUTI SIMUYENERA
KUPHA ANTHU ANZANU, KOMA INE
NDIKUTI MUKAKWIYIRA MBALE WANU
POPANDA CHIFUKWA CHENICHENI,
MULLINGU ADZAKUWERUZANI
NDITHU.

MATEYU 5:8, 21-22, 38-42, 43-44, 6:12; MARKO 1:34;


MUDAMVA KUTI MUNTHU
ASAMACHITE CHIGOLOLO, KOMA INE
NDIKUTI MUKAMUYANG'ANA KWAMBIRI
MKAZI, NKUMALAKALAKA MUTAGONA NAYE,
NDIYE KUTI MWACHITA NAYE KALE
CHIGOLOLO MUMTIMA MWANU.






ATSOGOLERI A
CHIPEMBEDZO
AMAONEKADI ABWINO
KUNJA KOKHA, KOMA
M'KATI MWAO NDI
ODZALA NDI UCHIMO.

ALI NGATI MANDA OPAKA LAIMU.
KUNJA AMAONEKA BWINO, KOMA
M'KATI MWAO NDI ODZALA NDI
MAFUPA A ANTHU AKUFA. NGATI
KULLINGAMA KWANU SIKUWAPOSA,
SIMUDZALOWA MU LIFUMU WANGA.

A man with a dark beard and mustache, wearing a white shirt and a yellow shawl, is shown in a dynamic, expressive pose. He has his right hand raised towards his chest and his left hand raised higher, with fingers spread. The background is a simple, light-colored wall with a dark shadow cast behind him. The style is reminiscent of a comic book illustration.

NJIRA YOPITA
KUCHIONENGEKO
NDI YOTAKASUKA
NDIPO AMBIRI
AKUYENDAMO.


INE NDINE KHOMO
LOLOWERA KUMWAMBA.
MUKALOWERA PA KHOMO
LIMENELI MUDZAPEZA MOYO
WOSATHA. MUKAYESERA
KULOWERA
KHOMO LINA MUDZAFERA
M'MACHIMO ANU.



NCHIFUKWA
CHIYANI UMACHIRITSA
PA TSIKU LA SABATA?
MOSE ADATILAMULA KUTI
TISAMAGWIRA NTCHITO
ILİYONSE PA SABATA.


ATATE
ANGA ADANDITUMIZA
M'DZIKO LAPANSI KUTI
NDIDZAGWIRE NTCHITO YAO.
NDIMACHITA ZOKHAZO
ZIMENE AMANDIENZA
KUTI NDICHITE.

UKUDZIYESA KUTI NDIWE
WOFANANA NDI MULLINGU.
KUMENKO NDI KUNYOZA
MULLINGU NDIPO WONYOZA
MULLINGU AMAYENERA
KUPHEDWA POPONYEDWA
MIYALA!



NDI CHIFUNIRO CHA ATATE
AKUMWAMBA KUTI ANTHU ONSE
APEMBEDZE NDI KULEMEKEZA
MWANA MONGA MOMWE
AMACHITIRA NDI ATATE.

NTHAWI IDZAFIKA PAMENE ONSE
AMENE ALI M'MANDA ADZAMVA MAU
ANGA NDI KULUKA KWA AKUFA, ENA KU
MOYO WOSATHA NDIPO ENA KU
CHILANGO CHOSATHA.




ZOONADI UYU NDI
MESIYA. POYAMBA
ANATIONETSA
ZUZIZWITSA NDIPO
TSOPANO AKUNENA
MOLIMBA MTIMA
ZIMENE AKUNENAZI.

AKUSIYANA
NDI ATSOGOLERI
ACHIPEMBEDZOWA.
AKUYANKHULA NDI
ULAMULIRO. AMENEYU
AMUPHA BASI.

NDIPITE
NDIKAMLUZE
MKAZI
WANGA.

MATEYU 5:27-28, 7:13-14, 28-29, 23:27-28;
YOHANE 5:18-19, 23, 29-30, 14:6




AKUBWERERANJI
USIKU UNO? KODI
AKUCHITA MANYAZI KUTI
ANTHU ADZAMUONA
AKUYANKHULA
NDI YESU?

NDIKAYANKHU
LA NAYE
PODUKA
MPHEPO.


AMBUYE,
MFARISI* UYU AFUNA
AKUONENI. NDI
MTSOGOLERI WA AYUDA,
MUNTHU WOFUNIKIRA
KWAMBIRI.

*MUNTHU WA M'GULU LINA LACHİYUDA LIMENE LINKADZIWIKA
KWAMBIRI POTSATA MIYAMBO YA AYUDA NCHOLINGA
CHOONETSA KUMVERA MULLINGU.



NGATI SUBADWANSO
KWATSOPANO SINGATHE
KUONA UFUMU WA
MULLINGU.

AMBUYE, IFE
ATSOGOLERI A AYUDA
TIMADZIWA KUTI INU NDINU
MPHUNZITSI WOCHOKERA KWA
MULLINGU, CHIFUKWA MUNTHU
SANGATHE KUCHITA
ZUZIZWITSA ZIMENE INU
MUMACHITA NGATI
MULLINGU SALI NAYE.



KODI MUKUTANTHALIZA
KUTI NDIYENERA KULOWA
M'MIMBA MWA AMAI ANGA
NDI KUTUKAMONSO
KACHIWIRI?

AI, CHOBADWA
MWA MUNTHU NDI
THUPI CHABE, KOMA
CHOBADWA MWA MZIMU
WOYERA NDI MZIMU.

KODI KUBADWA
KUMENEKU
KUMACHITIKA
MOTANI?



KUBADWA MWA
MZIMU KUMENE NDIKUNENA
KUMACHITIKA MODABWITSA
MONGA MPHEPO, KOMABE
TONSE TIMAKULANDIRA NDITHU.
UYENERA KUBADWANSO KUTI
UKALOWE MU UFUMU
WA MULLINGU.

MONGA MOMWE
MOSE ANAKWEZERA
NJOKA M'CHIPULULU,
MOMWEMONSO INE
NDIYENERA
KUKWEZEDWA.


NUMERI 21:5-9; YOHANE 3:1-14

KOMA ANTHU ANKAFWA
NJOKA ZIKAWALLUMA
CHIFUKWA ADACHIMWIRA
MULLINGU. AKAYANG'ANA
NJOKA YAMKLUWA
ANKACHIRITSIDWA
NTHAWI YOMWEYO.





INDE, NGAKHALE TSOPANO LINO ANTHU
ONSE AKUFA CHIFUKWA 'CHOLLUMIDWA' NDI
UCHIMO. KOMATU PA NTHAWI IMENEYI
NDIKWEZEDWA KUTI ANTHU ONSE AONE. MONGA
MOMWE ANTHU ANKACHIRITSIDWIRA M'CHIPULULU
MUJA AKAYANG'ANA NJOKA YAMKLIWA, ANTHU
OLLUMIDWA NDI TCHIMO ADZAPULLUMUTSIDWA
POKHULLUPIRIRA INE.//



CHONCHO MUKUNENA
KUTI KUBADWANSO
KWATSOPANO NDIWO
MANKHWALA A UCHIMO,
NDIPO KUTI
MUDZAKWEZEDWA PA
MTENGO KUTI
MUPULUMUTSE ANTHU
ONSE.



KODI KUBADWA
KWATSOPANOKU
KUDZACHITIKA
LITI?

NDIKADZAKWEZEDWA
KUTI ANTHU ONSE
AONE.

ASAMARIYA ANKAKHALA
PAKATI PA YERUSALEMU NDI
GALILEYA. AYUDA
SANKAYANJANA NDI
ASAMARIYA MWA NJIRA INA
ILİYONSE, NDIPO
SANKAFUNA NGAKHALE
KUDUTSA M'MIZINDA YAO,
POPEZA ANKAKHULUPIRIRA
KUTI ASAMARIYAWO ANALI
ODETSEDWA MU MZIMU.
TSIKU LINA YESU
ANADABWITSA OPHUNZIRA
AKE PONENA KUTI:



TIYENI,
NDIYENERA
KUDUTSIRA KU
SAMARIYA.



NDI CHIFUNIRO
CHA ATATE KUTI
NDIPITE KU
SAMARIYA.

AMBUYE, NDI
ANTHU ODETSEDWA,
MBUTUMA ZENIZENI! NDI
ANTHU OSAUKA NDIPO
MAKHALIDWE AO NDI
ACHABECHABE.

NTHAWI YA MASANA
ANAFIKA PA CHITSIME
CHIMENE CHINALI
KUNJA KWA MZINDA.



PITANI MUKAGULE
CHAKUDYA MUMZINDAMU.
NDIKUDIKIRANI PA CHITSIME
POMPANO.

KODI MUTSALA
NOKHANOKHA?

INDE, NDIYENERA
KUGWIRA NTCHITO
YA ATATE ANGA.



YESU ADATOPA, ANALI NDI LUDZU,
NDIPONSO ANKAMVA NJALA.
NGAKHALE SINALI NTHAWI IMENE
AKAZI ANKABWERA KUCHITSIMEKO,
MAI WINA WACHISAMARIYA
ANABWERA KUDZATUNGA MADZI.

YOHANE 4:1-8



KODI
MUNGANDIPATSEKO
MADZI AKUMWA
M'CHOTUNGIRA
CHANUCHO?

LIKADADZIWA
MPHATSO YA MULUNGU
NDI INE, UKADANDIPEMPHA
NDIPO NKADAKUPATSA
MADZI AMOYO.


HAA! NCHIFUKWA
CHIYANI INU, MYUDA,
MUKUPEMPHA MADZI KWA
INE, MAI WACHISAMARIYA?
NDIMAYESA KUTI INU
AYUDA MULIBE NAFE
KANTHU.



KUPATSA MADZI INE?
MULIBE CHOTUNGIRA NDIPO
CHITSIMECHI NCHAKUYA. MADZI
AMOYOWO MUWATENGA KUTI?

NDIYETU PATSENI
MADZI AMOYOWO KUTI
NDISADZAMVENSO
LUDZU.

MUKAMWA MADZI
A M'CHITSIME ICHI
MUDZAMVANSO LUDZU.
MADZI AMENE
NDIDZAKUPATSANI
ADZAKHALA MWA INU
NGATI MTSINJE WA
MOYO WOSATHA.



PITANI KAITANENI
MWAMUNA WANU KUTI
NDIDZAKUUZENI ZA
MADZI AMENEWA.


NDILIBE
MWAMUNA.

MWAKWATIWAPO
NDI AMUNA ASANU,
KOMA MWAMUNA
AMENE MUKUKHALA
NAYE TSOPANO
SIWANU.



ZOONADI
NDINU MNENERI
CHIFUKWA
MUKUDZIWA
TCHIMO LANGA
LAMSERI.

INU AYUDA
MUMAPEMBEDZA KU
YERUSALEMU NDIPO MAKOLO
ATHU AMAPEMBEDZA PA
PHIRI ILI. KODI PHIRI LENILENI
NDI LITI LOYENERA
KUPEMBEDZERAPO?



MULLINGU NDI MZIMU.
SAPEMBEDZEDWA M'MAKACHISI
OMANGIDWA NDI MANJA A ANTHU.
MULLINGU AKUFUNAFUNA ANTHU
AMENE ADZAKHULLUPIRIRA CHOONADI
NAPEMBEDZA IYE MU MZIMU.

TIKUDZIWA KUTI
MESIYA AKUBWERA
NDIPO AKADZABWERA
ADZATIULLULIRA
CHOONADI.

UKUYANKHULA
NDI MESIYA.






**NDIKAWAUZE
ANZANGA
ZIMENEZI!**

**YESU ADAKHALA KU
SAMARIYA MASIKU AWIRI
NDI KUMAPHUNZITSA
ANTHU MAU A MULLINGU.**

YOHANE 4:7-29, 40




TSIKU LINA YESU NDI OPHUNZIRA
AKE ANAIMA M'MBALI MWA
PHIRI LINA MOYANG'ANANA
NDI NYANJA YA GALIYEYA.

MUKAMAPEREKA
NDALAMA KWA ANTHU
OSAIKA, MUSAMAPEREKERA
POYERA POMWE ANTHU ENA
AKHOZA KUKLONANI.


ANTHU AMBIRIMBIRI
OCHOKERA M'MIZINDA
ANABWERA KUDZAMVA
ZOPHUNZITSA ZAKE.

MUKAMACHITA
ZACHIPEMBEDZO MWA NJIRA
YOTI AKUYAMIKIRENI NDI KUTI
ANTHU AKUSIRIRENI, MULLINGU
SADZAKUPATSANI MPHOTHO
KUMWAMBA. CHONCHO MUSAMALOLE
KUTI DZANJA LANU LAMANJA
LIDZIWE ZOMWE DZANJA LANU
LAMAZERE LIKUCHITA.




MUKAMAPEMPHERA,
MUSAMAKHALE NGATI
ANTHU ACHIPEMBEDZO
ACHINYENGOWA,
AMENE AMAPEMPHERA
POYERA KUTI ANTHU
ONSE AWAONE.

NDIPO INUYO MUKAMAPEMPHERA
MUSAMABWEREZABWEREZA MAU, MONGA
MMENE AMACHITIRA ATSOGOLERI ANU
ACHIPEMBEDZO, POPEZA AMAIMA M'MALO A
ANTHU AMBIRI KUTI ANTHUWO AONE ZA
KUDZIPEREKA KWAO.

A man with a beard and long hair, looking upwards with a thoughtful expression. He is wearing a dark garment. The background is a light blue sky with some faint clouds.


MUSAMATAYE
NTHAWI NDI MPHAMVU ZANU
NCHOLINGA CHOFUNA KULEMERA.
ANTHU OLEMERA ALI NDI MAVUTO
AMBIRI KUPOSA ALIYENSE, NDIPO
AMAKONDA CHUMA CHAO KWAMBIRI
KOTERO NKOVLITA KUTI
AKALOWE KUMWAMBA.

MUSADZIUNJIKIRE CHUMA
M'DZIKOLI, KOMA MUZISUNGA CHUMA
CHANU KUMWAMBA KUMENE CHIDZAKHALA
MPAKAMPAKA. SIMUNGATUMIKIRE MABWANA
AWIRI, MULLINGU NDI NDALAMA. ZOTSATIRA
ZAKE MUDZADANA NDI WINA NDI
KUKONDANA NDI WINAYO.




AMBUYE, KUKUDA, NDIPO
ANTHUWA AKHALA NAFE TSIKU
LONSE. MOSAKAIKA KONSE ALI
NDI NJALA, NDIPO KOTI
NKUKAGULA CHAKUDYA
NDI KUTALI.

AUZENI KUTI
AZIPITA KUTI
TSONO
AKADZIGULIRE
OKHA
CHAKUDYA.




AMBUYE, NACHI
CHAKUDYA KUTI
MUDYE. AMAI ANGA
ANANDIKONZERA KAMBA
WA BUREDI MSANU NDI
NSOMBA ZIWIRI.



LIZANI ANTHU
ONSE KUTI
AKHALE PANSI
KUTI TIWAPATSE
CHAKUDYA.

TIWAPATSANJI?

MATEYU 14:15, 6:1-7, 19-21



TIONE.
ZIONEKA
KUTI TILI NDI
NSOMBA NDI
BUREDİ.

BWEREKANI MADENGLU
KHUMI NDI AWIRI NDIPO
MUKONZEKERE
KUGAWA CHAKUDYA.

KOMA AMBUYE,
ZIMENEZI
SIZINGAKWANE
NGAKHALE MUNTHU
MMODZI, NANGA
NANJINANJI ANTHU
PAFUPIFUPI ZIKWI
ZISANUWA!



WODALITSIKA
NDINU, INU
AMBUYE MULLINGU
WATHU, MFUMU
YA DZIKO LONSE,
AMENE
MUMATIPATSA
CHAKUDYA
KUCHOKERA
M'NTHAKA.



AKUTANTHAUZANJI
POIKA CHAKUDYA
CHOCHEPACHO
M'DENGLU
LALIKULUKULULO?



**TAONANI!
CHAKUDYA
CHIMENECHI
CHACHOKERA
KUTI?**


MATEYU 14:19-21; LUKA 9:16-17




**TAMANDANI
MULLINGU!**

AMATIPATSA
CHAKUDYA
KUCHOKERA
KUMWAMBA...MO
NGA PA NTHAWI
YA MOSE.

AMAI
SAKAKHULLUPIRIR
A ZIMENEZI!



ANTHU ANATENGA
BUREDI NDI NSOMBA
KUCHOKERA
M'MADENGU AJA.
CHAKUDYA
CHINKANGOCHULLUKIRA
CHULLUKIRA.



AMBUYE, ANTHU
ONSE ADYA, KOMA
MADENGLI AKADALI ODZAZA.
SITINGATHE KUMALIZA
CHAKUDYA CHONSE.


SONKHANITSANI CHAKUDYA
CHOTSALA, KENAKA IWE NDI ANZAKO
MUKWERE CHOMBO KUPITA KU TSIDYA
LINA LA NYANJAYI. NDIKUTSATIRANI
NTHAWI INA. NDIKUPITA KU PHIRI
KUKAPEMPHERA.

YESU ANAPITA KU PHIRI
YEKHAYEKHA, NDIPO
OPHUNZIRA AKE ANAKWERA
CHOMBO KUPITA KU TSIDYA
LINA LA NYANJAYO.



MATEYU 14:20-23

YESU ANKAKONDA KUPITA
YEKHAYEKHA KU CHIPULULU
KUKAPEMPHERA.



OPHUNZIRA AJA ATAFIKA PAKATI PA
NYANJA, NAMONDWE WOOPSA
ANAIKA, NDIPO ANAYAMBA
KUCHITA MANTHA KUTI AMIRA.

SINDINAONEP
O NAMONDWE
WOIPA NGATI
UYU.

SITINGAPIRIRE
NAYE
NAMONDWE
AMENEYU.

A black and white comic book illustration showing a group of men in a boat. The men are dressed in traditional, heavy clothing, possibly shawls or robes. They appear to be in a state of distress or urgency. The background is filled with dark, swirling lines, suggesting a storm or a turbulent sea. A speech bubble is positioned in the upper left quadrant, containing the text 'TIMIRA!'.

TIMIRA!


***ONANI!
PAMADZIPO PALI
CHINA CHAKE!***



**NDI
MZUKWA!**

**NDI
MZUKWA!**

**NDI MUNTHU
AMENE
AKUYENDA
PAMADZIPO!**



AMBLIYE NGATI
NDINUDI, MUNDILOLE
NDIBWERE KWA INU POYENDA
PAMADZI PA, MONGA MOMWE
MUKUCHITIRA.

*PETRO,
NDINE,
USAOPÉ.*

BWERA
KWA INE,
PETRO.

MATEYU 14:24-29



NDIKUBWE
RA
AMBLIYE.

AI, PETRO!

PETRO ANKAYENDA
NDITHU PAMADZIPO
KUPITA KWA YESU.



PETRO ATAONA MAFUNDE
AKULLIAKULU SANATHENSO
KUONA YESU, ANACHITA
MANTHA.



MANTHA ANAONONGA
CHIKHULLUPIRO CHAKE,
NKUYAMBA KUMIRA.



**AMBUYE,
PULLUMUTSÉNI!**

MATEYU 14:29-30

PETRO,
UNAYAMBA
KUKAIKA
NANE.



YESU
ANAMUBWEZERET
SANSO PETRO
M'CHOMBO
MUJA, ONSE
AWIRI AKUYENDA
PAMADZI.




*PETRO,
UNAYENDA
PAMADZI!*



BATA,
CHETE.

YESU ANADZUDZULA
NAMONDWE NDIPO
MWADZIDZIDZI PAMADZIPO
PANADZA BATA.

MATEYU 14:31-33



CHOKANI KWA INE,
AMBUYE, PAKUTI
NDINE MUNTHU
WOCHIMWA.

ZOONADI INU
NDINU MWANA
WA MULLINGU.

AMBUYE
NDI
MULLINGU
WANGA.

KHRISTU
WA
ISRAELE.



PAMBUIYO
PAKE

MASIKU APHWANDOWA
KULI ANTHU AMBIRI. ANTHU
AMENEWA ABWERA KUCHOKERA KU
MAIKO ONSE, ENA ACHOKERA KU
IGUPTO NDI KU ROMA, KUMENE
NDI KUTALI KWAMBIRI.

TIYENI TIPITE
KU DZIWE ILO.


NDIKUKUMBUKIRA
KUTI WAKHALA
KUNO KWA
NTHAWI YAITALI.





KODI LIFUNA
UCHIRITSIDWE.


NDILIBE
MUNTHU WOTI
NKUNDITHAND
IZA.



DZUKA, YALULA
MPHASA YAKO,
NDIPO YENDA.

NDINU *YESU*,
SICHONCHO?
NDIDAMVA ZA
ZUZIWITSA
ZANU.

YOHANE 5:1-8



MASEWERATU.
MUNTHU AMENEYU WAKHALA
ALI WOLLUMALA KWA ZAKA
38.

LERO NDI SABATA
LATHU LOYERA. ALIBE
MPHAMVU ZOSOKONEZERA
MTENDERE WATHU.



NDIKUMVA KUTI PALI
KAGULU KENA KA ANTHU
KAMENE KAKUFUNA KUMUPHA.
WANYANYA KUKOPA ANTHU.

KODI YESUYU
AKUGANIZA KUTI
NDANI, MESIYA?

INDE, ALI NDI
ANTHU AMENE
AMATSIMIKIZA KUTI
ANGATHE KUCHITA
ZUZIZWITSA.





**AKUDZUKA
NDITHU!**

NZOSATHEKA!



AMBUYE
ALEMEKEZEKE!
ZAKA ZONSE
ZIMENE NDAKHALA
NDIKUVUTIKAZI!

YESU NDI
MESIYA!



NCHIFUKWA
CHIYANI
UKUCHIRITSA
PA SABATA?

NCHIFUKWA
CHIYANI
UKUCHIRITSA
PA SABATA?

NKOLOLEDWATU KUTULUTSA
NG'OMBE YOMWE YAGWA M'DZENJE
PA TSIKU LA SABATA. KODI INE
NDIKUSWA LAMULO POCHIRITSA
MUNTHUYU PA SABATA?

ATATE ANGA
AMAGWIRA NTCHITO
PA SABATA, NDIPO
INE NDIMATSANZIRA
ATATEWO.

LUKA 14:5-6;
YOHANE 5: 9-17



**MGWIRENI!
TIYENERA
KUMUGENDA
NDI MIYALA
KUTI AFE.**

**AKUTI MULLINGU
NDI ATATE AKE.
NDIYE KUTI
AKUDZISANDUTSA
WOFANANA NDI
MULLINGU.**

MUPHENI!




KODI MUFUNA
MUMUPHE CHIFUKWA
CHOCHIRITSA PA
SABATA?

SANANENE
CHILICHONSE
MOTSUTSANA NDI
MALAMULO.


AKUYANKHULA
MOTSUTSANA
NDI MALAMULO
ATHU.

MVERANI
CHIMENE ATI
ANENE.




MVERENI. MUKUZIZWA
CHIFUKWA NDACHITA
CHOZIZWITSA CHIMODZICHI.
MUDZAONA ZOZIZWITSA
ZAZIKULU ZOPOSA ICHI. MONGA
ATATE ANGA AMAITSA ANTHU
KWA AKUFA, MOMWEMO
WANDIPATSA INE MPHAMVU
ZOMWEZO. ATATE ANGA
ANDIPATSA MPHAMVU ZONSE
ZOLAMULIRA DZIKOLI.

LINGAUPEREKE
BWANJI MOYO
WOSATHA?



NGATI
SIMUNDILEMEKEZA
INE NDIYE KUTI
SIMULEMEKEZA MULLINGU.
ZONADI NDIKUKUUZANI,
AMENE AMAKHULLUPIRIRA
INE AMAKHULLUPIRIRA
AMENE ANANDITUMA,
NDIPO ADZAKHALA NDI
MOYO WOSATHA.


LINGAUPEREKE
BWANJI MOYO
WOSATHA?



IDZAFIKA NTHAWI PAMENE ANTHU
AKUFA ADZAMVA MAU ANGA NDIPO
ADZATULLIKA M'MANDA MWAO. AMENE
ANACHITA BWINO ADZAIKA NDI KUPITA KU
MOYO WOSATHA, KOMA AMENE ANACHITA
ZOIPA ADZAPONYEDWA KU CHILANGO
CHOSATHA M'NYANJA YA MOTO.

UMENEWO
NDI MWANO;
PALIBE MUNTHU
AMENE ANGALITSE
ANTHU AKUFA. NDI
MULLINGU YEKHA
AMENE AKHOZA
KUPEREKA MOYO
WOSATHA.

YOHANE 5:18-29



SIMUKUNDIKHULUPIRIRA,
KOMA YOHANE ANANENERA ZA
KUBWERA KWANGA MONGANSO
MALEMBO AMANENERA.
FUNAFUNANI M'MALEMBO,
PAKUTI ANENERI AMBIRI
ANANENA ZA INE.


MUSAGANIZA KUTI
INE NDIDZAKUTSUTSANI
PAMASO PA MULINGU,
MALAMULO A MOSE, AMENE
MWALEPHERA KUWASUNGA,
NDIWO ADZAPEREKA LIMBONI
WOKUTSUTSANI.



AKUFUNA KUPHA MUNTHU
AMENEYU, KOMATU AKUYANKHULA
MWAMPHAMVU NDIPO IWOWA PALIBE
CHIMENE AKUCHITA. KODI ATSOGOLERIWA
AKUDZIWA KUTI AMENEYU NDIYEDI
KHRISTU, MESIYA WA ISRAELE?



ALEMBI A MALAMULO ACHIYUDA
AMAPHUNZITSA KUTI SITIDZADZIWA KOMWE
MESIYA ADZACHOKERE, KOMA TIKUDZIWA
KUTI MUNTHU UYU NDI MWANA WA MMISIRI
WA MATABWA WA KU GALILEYA.



MUKUTI MUMANDIDZIWA
NDIPO MUMADZIWANSO KUMENE
NDIMACHOKERA. SINDINABWERE
M'DZIKO LAPANSI MWAKUFUNA
KWANGA. ATATE ANGA NDIWO
ADANDITUMA, KOMA ATATE
ANGAWO SIMUWADZIWA; KOMA
INE NDIMAWADZIWA NDIPO
ANDITUMA KWA INU.

**WATIMVER
A BWANJI?**



AMADZIWA
ZINTHU ZONSE.

AMENEYU NDI
MESIYA AMENE
KUBWERA KWAKE
KUDANENEDWA
KALE!

KODI MUKUYEMBEKEZA
MESIYA WODZACHITA
ZUZIWITSA ZOPOSA ZIMENE
MUNTHUYU AKUCHITA?




THAMANGANI,
KAMANGENI MUNTHU
WAMWANOYO.

PANOPA
ZIKHOZA
KUTIVUTAPO.

ANTHU
AKUMUKHULUPIRIRA.
TIYENERA
KUMUKHALITSA
CHETE.

YOHANE 5:30-39, 45,
6:42-43, 7:25-32, 40-41



NDI ODALA AMENE
AKUMVA LUDZU LA
CHILINGAMO, POPEZA
ADZAKWANIRITSIDWA.

MUNTHU WINA AKAMVA
LUDZU, ABWERE KWA INE KUTI
ADZAMWE. MZIMU WOYERA
ADZAKHALA MWA IYE NGATI CHITSIME
CHAMADZI CHOTUMPHUKIRA KU
MOYO WOSATHA.

NDI ODALA ANTHU
ODZETSA MTENDERE,
PAKUTI ADZATCHEDWA ANA
A MULLINGU. KONDANI
ADANI ANU NDIPO
MUZIWADALITSA.

SAKLIYANKHULA
NGATI
WACHIFWAMBA.

AKUTI NDIYE
WOKWANIRITSA
UNENERI WA
ZAKA 4000.



NCHIFUKWA CHIYANI
SIMUNAMUBWERETSE KWA
IFE? ANAIMA KUTSOGOLO,
PAFUPI PENIPENI NDI INU.
NCHIFUKWA CHIYANI
SIMUNAMUGWIRE.

PALIBE
MUNTHU AMENE
ADAYANKHULAPO
MONGA MUNTHU
AMENEYU.


AMAYANKHULA ZA
KUKONDANA NDI
KUKHULULUKIRANA.



HAA, KODI NANUNSO
WAKUNYENGANI? KODI NDANI
PAKATI PA ATSOGOLERI OPHUNZIRA
NDI AFARISI AMENE AMUKHULUPIRIRA?
YESU AMENEYU AYENERA KUFA.

NIKODEMO, AMENE ADAABWERA
KWA YESU USIKU, ANAYANKHULAPO.

MATEYU 5:6, 9;
YOHANE 4:14, 7:45-52



KODI MALAMULO ATHU
AMAWERUZA MUNTHU ALIYENSE,
MUNTHU WOIMBIDWA
MLANDUYO ASANANENE
MBALI YAKE?

NIKODEMO, KODI NAWENSO NDIWE
MMODZI MWA ANTHU A KU GALILEYA AMENE
AKUTSATA MUNTHUYU? FUFUZA M'MALEMBO,
PAKUTI MESIYA SADZACHOKERA KU GALILEYA.
AYENERA KUCHOKERA KU BETELEHEMU WA
YUDEYA, NDIPONSO AYENERA KUKHALA
MWANA WA DAVIDE.




AMANAMIZA
ANTHU WAMBA
NDI BODZA
LAKELO.

AONEKA KUTI
ALI NDI YANKHO PA
CHILICHONSE.

BWANJI
TITUMIZE MMODZI MWA
MALOYA OCHENJERA
KWAMBIRI KUTI
AKAMUSOKONEZE.



LOYA WOTERO
NDIKUMUDZIWA. NDI
WOCHENJERA KOMANSO
ALIBE CHIFUNDO.




LOYA AKUBWERA
KUDZAYESA YESU.

MPHUNZITSI,
NDICHITE CHIYANI
KUTI NDIKAPEZE
MOYO WOSATHA?

MALAMUL
O AMATI
CHIYANI?

AMATI UZIKONDA AMBUYE
MULLINGU WAKO NDI MTIMA
WAKO WONSE, MOYO WAKO WONSE,
MPHAMVU ZAKO ZONSE, NDI NZERU
ZAKO ZONSE, NDIPONSO KUTI
UZIKONDA MNZAKO MONGA
MOMWE UMADZIKONDERA
IWE MWINI.



WAYANKHA BWINO ZEDI.
CHIKONDI NDICHO
CHIMAKWANIRITSA MALAMULO
ONSE. NGATI UKONDA MNZAKO
MONGA MOMWE UMADZIKONDERA
IWE MWINI, UDZAKONDWERETSA
MULLINGU.

INDE, KOMA NANGA
MNZANGAYO NDANI?
MUKUTANTHAUZA ALIYENSE
NGAKHALE AROMA,
AKUNJA AJA?


NDIKULUZA
NTHANO:



MUNTHU AMENE
ANKACHOKERA KU YERUSALEMU
KUPITA KU YERIKO ANAVULAZIDWA
NDI ACHIFWAMBA PA NJIRA,
ANAMUVULA ZOVALA ZAKE,
NKUMUSIYA ATAKOMOKA.

PAMENE WANSEMBE
ANKADUTSA NJIRA
YOMWEYO, KUONA
MUNTHU UJA ALI GONE,
ANAMULAMBALALA NDIPO
SANAIME KUTI
AMUTHANDIZE.

LUKA 10:25-31



CHIMODZIMODZINSO MLEVI,
MUNTHU WOSANKHIDWA KUTUMIKIRA
M'NYUMBA YA MULLINGU, ANALAMBALALA
NDIPO ANANGOIMA PATALI KWA
KANTHAWI KOCHIPA KUYANG'ANA
MUNTHU WOVULALAYO, KOMA
SADAMUTHANDIZE.

KODI TINGAPINDULENJI
KUNGONENA CHABE KUTI
TIMAKONDA ANZATHU KOMA
OSAONETSA NTCHITO ZA CHIKONDI?
NGATI SUKONDA MNZAKO NDIYE
KUTI SUKONDA MULLINGU.


KENKA MSAMARIYA
ANKADUTSA NJIRA YOMWEYO;
MUNTHU AMENE AYUDA AMAMUNYOZA
NKUMATI NDI WODETSEDWA. ATAONA
MUNTHU WOVLALAYO, WOVLIDWA
ZOVALA ZAKE, ALI GONE MU MSEU,
SANALABADIRE ZOTI MUNTHUYO
ANALI MYUDA.



MSAMARIYA
ANAMUMVERA CHISONI,
NDIPO ANAIMA
KUTI AMUTHANDIZE.



MSAMARIYA UJA
ANATSIKA ZILONDA
ZA MUNTHU UJA
NAZIMANGA NDI NSALU
ZOMANGIRA ZILONDA.
CHIKONDI CHAKE
SICHINALI PA MAU
CHABE, KOMA PA
ZOCHITA.



KENAKA MSAMARIYA
UJA ANAMUKWEZA MUNTHUYO
PA BULLU WAKE NAPITA NAYE
KU MALO OTI AKASAMALIDWE,
KOMWE ANAKAYENERA
KUPUMA KUTI ACHIRE
BWINOBWINO.

ZILI BWINO
TSOPANO.
NDAKUPEZA.
POSACHEDWAPA
UKAPUMULA
POGONA PABWINO.



NDILIPIRIRATU
NDALAMA ZA CHAKUDYA
NDI MALO OGONA,
NDALAMA ZA PA MILLINGU
IWIRI. NGATI MTENGO
WOMUSAMALIRA UKULIRAPO,
NDIDZALIPIRIRA
NDIKAMADZADUTSANSO
POCHOKERA KOMWE
NDIKUPITAKU.

LUKA 10:32-35




UNANDIFUNSA KUTI
MNZAKO NDANI. NDIUZE TSOPANO,
NDANI PAKATI PA ANTHU ATATUWA
ANALI MNZAKE WA MUNTHU
WOVULALAYU?

AMENE
ANAMUCHITIRA
CHIFUNDOYO.

ZOSATHEKA!



NDIYETU PITA
NDIPO LKACHITE
MONGA ANACHITIRA
MSAMARIYAYO.
LKAKONDE
MNZAKO.



WOPUSA!
MCHOTSENIPO
PAMENEPO YESU
ASANAMUTEMBENUZE
MTIMA.

ICHI NDI
CHIPHUNZITSO CHAMISALA
NDITHU! SIZINGATHEKE. ANTHU
ENA, NGAKHALE UTAWACHITIRA
CHIFUNDO, SABWEZERA
CHIFUNDO.



MATEYU 5:43-44;
LUKA 10:36-37

MUDAMVA KUTI MUZIKONDA
ABWENZI ANU OKHA NDI KUMADANA NDI
ADANI ANU, KOMA INE NDIKUTI KWA INU,
MUZIKONDA ADANI ANU, MUZIWADALITSA
AMENE AMAKUTEMBERERANI, MUZIWACHITIRA
ZABWINO AMENE AMADANA NANU, NDIPO
MUZIWAPEMPHERERA AMENE AMAKUNYOZANI
NDI KUKUZUNZANI.



<https://goodandevilbook.com/>